Kalata ya No. 12

# UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

MALANGIZO NDI CHILIMBIKITSO KUCHOKERA M'BAIBULO KUPITA KWA AMENE AKULALIKIRA UTHENGA WABWINO

## MAZUNZO A KHRISTU

*(Nkhani yotsatirayi ifotokoza za kukhomedwa pa mtanda kwa Khristu monga momwe adafotokozera m'mabuku pa Mateyu 27, Marko 15, Luka 23 ndi Yohane 19)*

Yesu anaperekedwa kwa adani ake, nagwidwa, nazengedwa mlandu ndipo anaweruzidwa kuti apachikidwe. Kenaka Yesuyo anamuvula zovala zake namuchita chipongwe pamene asilikali achiroma anamuzunza namukwapula kwambiri. Kukwapula kotere kunali chilango choyamba chimene chimayenera kuperekedwa kwa munthu amene akukakhomedwa pamtanda ndipo cholinga chake chinali chakuti munthuyo afooke ndipo asatenge nthawi kuti afe. Aroma amagwiritsa ntchito mkwapulo waufupi wokhala ndi zikopa zingapo kumene amamangirirako tizitsulo ting'onoting'ono takuthwa kapena zidutsa zakuthwa za mafupa a nkhosa. Mmene Yesu amamukwapula, amatema nkhungu lake ndipo magazi anatuluka m'thupi mwake. Ndipo akamapitiriza kukwapulako, mitsempha ndi minofu ya pamsana pake inali kutemedwa.

Pofuna kumuchita chipongwe, asilikali aja anamuveka Yesu mkanjo wofiira pa thupi lake la magazi ndi chisoti chaminga pa mutu wake. M'malemba nthawi zambiri minga zimayimira uchimo ndipo tsopano Mfumu ya Mafumu inasenza uchimo wa dziko lapansi. Anamupatsa ndodo m'dzanja lake namuseka akumugwadira



namanena, "Tikuoneni, Mfumu ya Ayuda!" Asilikali anamukwapula pa mutu ndipo anamva ululu. Adamuseka namulavulira malovu.

Malingana ndi mwambo wa nthawi imeneyo, Yesu anasenzetsa mtanda pamsana pake. Manja ake otambasuka anawamangirira ku mtanda wolemera pakati pa 35-56 kilogalamu. Yesu adapita naye ku Gologota kukaphedwa. Chifukwa chakufooka, Yesu anadzandira popeza mtanda unali wolemera ndipo sanathe kupitirira. Munthu wina wotchedwa Simoni anamuthandiza kunyamula mtanda wakewo.

Nthawi itakwana 9:00 m'mawa (ola lachitatu), Yesu adamugwetsa pansi ndipo manja ake anawakhomera pamtanda ndi misomali. Adaika chikwangwani pamtanda chimene pomwe adalemba kuti "YESU MNAZARAYO, MFUMU YA AYUDA." Mtanda adauimika ndipo misomali adaikhomanso ku pamapazi ake.

Kukhomedwa pa mtanda idali njira yowawa ndi yochititsa manyazi kwambiri yophera munthu. Njirayi idali yoyenera akapolo, alendo, oukira ndi mbava zoopsa. Cholinga chake chidali choti munthu amve ululu wambiri ndiponso kuzunzika. Mbava ziwiri adazipachika pamodzi ndi Yesu kumbali zonse ziwiri.

*(Yapitirira pa tsamba 2)*


| Mawu a Mkonzi | Kusanthula Mau a Mulungu: Mwambo wa mgonero wa ambuye | Nkhani yothandiza pa kusanthula Baibulo: Mwambo wa mgonero wa ambuye | Mafunso ndi Mayankho | Kodi Mukudziwa? Mau a pa Nyengo yake |
|---|---|---|---|---|
| 3 | 4 | 5-6 | 7 | 8 |

# ZIMENE BAIBULO Limaphunzitsa za...

**Mau a Mulungu**
2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35
**Ubale wa Chikondi**
Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11
**Kulapa**
Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10
**Kubadwa mwatsopano**
Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6
**Kupulumuka ku uchimo**
1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11
**Chidzalo cha Mzimu Woyera**
Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8
**Chiyero**
Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22
**Ufumu wa Mulungu**
Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36
**Mpingo**
Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18
**Umodzi**
Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4
**Maskaramenti**
Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17
**Machiritso**
Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16
**Chiyero cha Banja**
Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11
**Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena**
1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5
**Masiku omaliza**
2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46
**Kukhala mwa mtendere**
Luk. 6:27-29; Luk. 18:20
**Kupembedza**
Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17
**Kulalikira Uthenga Wabwino**
Mrk. 16:15

*(Kuchokera pa tsamba 1)*

Atamupachika pa mtanda akumva ululu, atamuzunza m'mnjira zosiyanasiyana, Yesu adayang'ana khamu la anthu lija napemphera, "Atate, muwakhululukire iwo, pakuti sadziwa chimene achita." Ngakhale Yesu adali ndimphamvu ya kuitana angelo kudzamuombola, adalolera kuti aperekedwe ngati nsembe chifukwa cha chikondi chake chachikulu pa anthu. Nthawi ya 12 koloko masana (ola lachisanu ndi chimodzi), dzuwa lidabisika ndipo mdima udagwa padziko lonse kwa maola atatu.

Kwa opachikidwawo, kupuma kudali kovuta. Thupi linkalendewera chifukwa cha misomali. Okhomedwayo kuti apume bwino amayenera kunyamula thupi lake. Minofu imang'ambika ndipo pamakhala ululu wosaneneka m'mitsempha ndipo zilonda zomwe zimayamba kupola zimatsekukanso.

Mumdima, pafupifupi 3 koloko madzulo (ola lachisanu ndi chinayi), Yesu adafuula mokweza nati, "Atate, m'manja mwanu ndipereka mzimu wanga." Yesu akumwalira, chinsalu chotchinga cha mkachisi chinang'ambika pakati kuchoka pamwamba mpaka pansi; ndipo panali chivomerezi chachikulu. Anthu onse tsopano angathe kufika kwa Mulungu kudzera m'mwazi wa Mwana Wake.

Yesu anazunzika nafa imfa yowawa kuti dziko lapansi lipulumuke chifukwa cha kudzipereka kwake. Msilikali, ataona kuti Yesu wamwalira, anabaya m'nthiti mwake ndipo munatuluka magazi ndi madzi. Mwina Satana amaganiza kuti wapambana chifukwa Mesiya tsopanso adali atamwalira...koma tsiku Lamulungu linafika! Yesu adauka mwachigonjetso ndipo ali ndi moyo ku nthawi za nthawi.

-mws

## UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

*Uthenga Wabwino wa Choonadi* ndi uthenga wa mkalata umene umasindikizidwa m'dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwakhazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choonadi cha Mau a Mulungu. Kalata uyu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zoona za Baibulo zimene zakhazikitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawo amene ali muyeso wovomerezeka wa chikhulupiriro. Amaphunzitsa chipulumutso ndi mamasulidwe kuchokera ku uchimo kudzera mu ntchito ya maomboledwe ya mwa Yesu Khristu; komanso kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kumene kumatsatirapo. Ndipo kumatithandiza kuti titsogolere, tiwongolere ndi kuwapatsa ena mphamvu; komanso tikhale ndi chiyero choonekera pa gawo lililonse la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi wa anthu a Mulungu. Utumiki wovomerezeka wa kwa Mulungu uli mu mwa anthu amene ubale wao wachikondi wazikika pa choonadi.

Akonzi: Michael & Rene Smith

## KUTI MULANDIRE NAWO KALATAYI

*Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi* uthenga wa kalata umene timasindikiza miyezi itatu ililyonse molingana ndi chitsogozo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi mwaulere pa email, pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa www.thegospeltruth.org. Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma email a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mkonzi.

## KUTI MUTIPEZE

Uthenga Wabwino wa Choonadi imasindikizidwa mu maiko osiyanasiyana kuti igawidwe m'maikowo. Ntchito yosindikiza kalatayi komanso mautumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zopereka zaufulu zoperekedwa mdzina la mpingo wa Mulungu.

The Gospel Truth, 605 Bishops Ct., Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

# Mau a Mkonzi



*Pamene ndiona mwaziwo ndidzapitirira inu, ndipo sipadzakhala mliri wakukuononganí ….* —Eksodo 12:13

Tithokoza Mulungu chifukwa cha mwazi wake! Pamene mngelo wa imfa anaona mwazi utapakidwa pa mphuthu za nyumba za Aisrayele ku Aiguputo, anapitirira nyumbazo. Tikadzaima ku mpando wachiweruzo wa Mulungu, ndipo akadzaona mwazi wa Mwana Wake, tiomboledwanso ku imfa yosatha.

Muli mphamvu m'mwazi wa Yesu wopulumutsa ku dzenje lozama kwambiri la tchimo. Munthu akakhazikika mu mphamvu za thupi ndipo aona kuti palibe njira yakuti akhoza kukhala m'moyo wachiyero, chonde musaiwale kuti mwazi wa Yesu ungayeretse ngakhale munthu woipitsitsa. Ngakhale Yesu adamwalira pafupifupi zaka 2,000 zapitazo, mwazi wake ukadali wamphamvu monga kale.




Gawo lino, titsiriza maphunziro athu a zolamulidwa poona za mutu wa mgonero wa Ambuye. M'Chipangano Chakale, nyama zimaperekedwa ngati nsembe pofuna kuti machimo akhululukidwe. "Pakuti sikutheka kuti mwazi wa ng'ombe zamphongo, ndi mbuzi ukachotse machimo" (Ahebri 10:4). Khristu adadzipereka yekha ngati nsembe yangwiro ndipo pamene anakhetsa mwazi wake tipezapo mphamvu yakukhala kopanda tchimo. Ndikumbukira nthawi zambiri ndimafuna kukhetsa misozi panthawi ya mgonero ndikamakumbukira za nsembe yailuku ya Khristu. Chikondi chake ndichachikulu ndipo adalipira dipo loposa kuti tipeze chipulumutso.

Dziko lathu limakondwerera kwambiri khrisimasi ndipo anthu ambiri amasangalala kubadwa kwa Khristu pa nyengoyi. Nkofunika kudziwa kuti Khristu sadabadwe mwezi wa Disembala ndiponso kuti sadatilamule kuti tizikondwerera kubadwa kwake. Yesu adalamula anthu ake kuti azikumbukira imfa yake mwa mgonero wa Ambuye. Ngakhale kuti Baibulo silinena za nthawi yoyikika pa chaka, chimakhala chinthu cha mtengo wake pamene mipingo ikhala ndi mwambo wa mgonero pa tsiku Lamulungu limene Yesu anauka kwa akufa.

Miyambo ndi zizindikiro zonse nzofunika pamene tikuchita mwambo wa mgonero wa Ambuye. Ndidziwa anthu ambiri samwera chikho chimodzi cha mgonero ndipo amafuna kuti aliyense amwere chikho chake. Sindidamvepo za munthu amene adadwala chifukwa chomwera chikho chimodzi pa mgonero. Ndidamwa ndi magulu ambiri a anthu amene adali ndimatenda osiyanasiyana ndipo sindinadwale.

Madzi a zipatso za mphesa adawagwiritsa ntchito m'Baibulo nthawi ya mgonero wa Ambuye. Ngakhale ichi ndi chizindikiro chabwino, Ndakhala ku malo kumene mphesa sizimapezeka. Timagwiritsa ntchito zinthu zamadzi zosiyanasiyana. Pa malo ena tidasakaniza soda ndi juisi amene amapezeka m'deralo. Ndikhulupirira Mulungu adalemekeza mwambo umenewu. Ndi dalitso loposa kutenga gawo pa mazunzo a Ambuye wathu. "Ambuye, timayanjana nanu m'mazunzo…."

Michael W. Smith

April 2015

# MLOZO WA KUSANTHULA BAIBULO

## MUTU: MWAMBO WA MGONERO WA AMBUYE

**Kuwerenga Mawu:** *Pakuti nthawi zonse mukadya mkate uwu ndi kumwera chikho, mulalikira imfa ya Ambuye kufikira akadza Iye.* —1 Akorinto 11:26

**Chidule:** Mgonero wa Ambuye ndi lamulo la m'baibulo limene lidakhazikitsidwa ngati chikumbutso cha mazunzo ndi imfa ya Yesu Khristu amene thupi lake linachekedwa ndipo mwazi wake unakhetsedwa pofuna kupulumutsa anthu.

**Werengani:** Mateyu 26:17-30; 1 Akorinto 11:20-34 (Santhulani: Luka 22:7-22; Marko 14:12-26).

**I. Mwambo udakhakazikitsidwa nthawi ya Paska**
- A. Eksodo 12:12-15 Paska ku Aiguputo.
- B. Mateyu 26:17-20 Phwando la mkate wopanda chotupitsa.
- C. Luka 22:7-16 Paska wakonzedwa.

**II. Unakhazikitsidwa ndi Khristu**
- A. Mateyu 26:26-29 Yesu adyetsa mgonero akuphunzira ake.
- B. 1 Akorinto 11:23 Cholandiliridwa kwa Ambuye.

**III. Cholinga cha Mgonero**
- A. Chikumbutso cha Chipangano Chatsopano
- B. 1 Akorinto 11:24b,25b "Chikumbukiro changa."
- C. 1 Akorinto 11:26 Kuonetsa imfa ya Ambuye.

**IV. Chizindikiro la Mkate**
- A. Mateyu 26:26 Thupi la Khristu.
- B. 1 Akorinto 11:24 Thupi lonyemedwa la Khristu.
- C. 1 Akorinto 10:17 Mpingo - thupi la Khristu.
- D. 1 Akorinto 5:6-8 Mkate wopanda chotupitsa.

**V. Chizindikiro cha Chipatso cha Mphesa**
- A. Mateyu 26:28-29 Mwazi wokhetsedwa wa Khristu.
- B. 1 Akorinto 10:16 Chiyanjano cha mwazi.
- C. 1 Akorinto 12:13 Kumwa mwa Mzimu umodzi.

**VI. Machitidwe oyenera a Mgonero wa Ambuye**
- A. Marko 14:22 Yesu anatenga mkate, naudalitsa, naunyema ndipo anawapatsa.
- B. Marko 14:23 Yesu anatenga chikho, nayamika, nachipereka kwa iwo ndipo iwo onse anamweramo.
- C. Onaninso: 1 Akorinto 11:23-26.

**VII. Mawu otsiriza a Mgonero wa Ambuye**
- A. Mateyu 26:30 Adayimba nyimbo.
- B. Marko 14:26 Adayimba nyimbo nachoka.

**VIII. Kuchita Mgonera kosayenera ku Akorinto**

1 Akorinto 11:20-22, 34 Mpingo unakhazikika pa kudya kwa nthawi ya mgonero osati ngati mwambo wa chikumbutso.

**IX. Lamuo kwa Okhulupirira**
- A. 1 Akorinto 11:27-28 Aliyense adziyese yekha.
- B. 1 Akorinto 11:29-32 Zotsatira za kudya mgonero kosayenera.

**X. Mpingo uyenera kusunga Lamulo**
- A. Mateyu 28:20 Tsatirani zinthu zonse.
- B. 1 Akorinto 11:2 Sungani malamulo onse.
- C. 1 Akorinto 11:25 Chitani ichi.

**Kumaliza:**

Koma munthu adziyese yekha, ndi *kotero* adye mkate, *ndi* kumwera chikho.

—1 Akorinto 11:28



*Zofunikira pokonza*

### Mkate wopanda chotupitsa

*Mkate wopanda chotupitsa ngosavuta kupanga. Zofunika popanga mkatewu ndizo fulawo ndi madzi.*

*Zofunika:*

**Kapu imodzi kapena imodzi ndi hafu ya ufa wa fulawo**

**Kapu imodzi ya madzi**

Ikani fulawo m'mbale. Pang'onopang'ono thirani madzi ku fulawo mukuvundula mpaka zilimbe ngati nsima. Thirani madzi kapena fulawo mpaka phala litalimba kuti mupange mkate ndi manja amene ali ndimafuta.

Ikani mchiwaya cha mafuta. Otchani m'moto wa uvuni wotentha 65°C kwa mphindi 15 mpaka zitapsa.



*"Ichi ndi thupi langa la kwa inu; chitani ichi chikhale chikumbukiro changa."*

1 Akorinto 11:24

# MWAMBO WA MGONERO WA AMBUYE

*Nkhani yothandiza pa kusanthula Baibulo*

**PASKA YA M'CHIPANGANO CHAKALE**

Pafupifupi zaka 3,500 zapitazo, Mose ndi ana a Aisrayele anali paulendo waukulu kutuluka mu ukapolo ku dziko la Aigupto. Mulungu adauza anthu ake kupereka nsembe ya nkhosa yopanda chilema ndi kuika mwazi wa nkhosa pa mphuthu za zitseko zawo. Usiku uja, mngelo wa imfa anayendayenda m'dziko lonse la Aiguputo napha mwana aliyense wachisamba m'makomo. Padali chiombolo ku imfa kwa amene adapaka mwazi wa nkhosa. Paska idaikidwa kuti chaka ndi chaka adzikumbukira chipulumutso chodabwitsachi (Eksodo 12:12-15).

**YESU AKHAZIKITSA MWAMBO WA MGONERO**

Patatha pafupifupi zaka 1500, Yesu ndi akuphunzira adakhala pansi kudya Paska (Luka 22:7-16). Yesu adadziwa kuti m'maola ochepa adzapachikidwa pa mtanda ngati nkhosa yothiridwa nsembe chifukwa cha machimo a anthu. Yesu adatenga mkate wopanda chotupitsa ndi chikho cha vinyo ndipo anachita mwambo woyamba wa mgonero (Mateyu 26:26-29). Yesu adakhazikitsa mwambowu ndipo Paulo mtumwi adatsimikiza za mwambowu. "Pakuti ine ndinalandila kwa Ambuye chimenenso ndinapereka kwa inu…" (1 Akorinto 11:23).

Litatha dongosolo la Paska, Yesu adakhazikitsa chikumbutso m'nthawi ya Chipangano Chatsopano. Munthu adzapulumuka ku imfa ya muyaya pokhapokha wapakidwa ndi mwazi wa nkhosa amene ali Yesu Khristu. Chiombolo chodabwitsa chimene aliyese anapeza kudzera ku mwazi wa nkhosa Yesu Khristu. Yesu adauza ophunzira ake kuchita mwambo wa mgonero "kuti chikhale chikumbukiro changa" (1 Akorinto 11:24b). Pamene anthu a Mulungu akuchita mwambo wa mgonero wa Ambuye, ichi ndi chikumbutso chowathandiza kuti sayenera kuiwala ululu ndi mazunzo a Mpulumutsi. "Pakuti nthawi zonse mukadya mkate uwu ndi kumwera chikho, mulalikira imfa ya Ambuye kufikira akadza iye" (1 Akorinto 11:26).




**MKATE UIMIRA THUPI LA KHRISTU**

Mgonero wa Ambuye ndi mchitidwe m'Chipangano Chatsopano chimene chili chisonyezo chachikulu pakuchita mwambowu. Yesu adagwiritsa ntchito mkate wopanda chotupitsa wa Paska nati, "Ichi ndi thupi langa la kwa inu; chitani ichi…" (1 Akorinto 11:24). Yesu adamukhomera pa mtanda ndiponso anamubaya ndi mkondo. Thupi lake linamenyedwa kuti tipulumuke. Mkate ndi chizindikiro cha thupilo limene lidakhomedwa pamtanda. Mkate wopanda chotupitsa ndi chizindikiro m'mawu a Mulungu cha thupi la Khristu, Mpingo wa Mulungu. "Pakuti ndife ambiri thupi limodzi: pakuti ife tonse titengako ku mkate umodzi" (1 Akorinto 10:17). Popeza mkate umakhala wopanda chotupitsa ndi wosasanthika, ngala zambiri za tirigu zimalumikizana pamodzi kupanga mkate umodzi wosagawikana. Anthu osiyanasiyana amalumikizika pamodzi m'thupi limodzi akasinthika ndi mphamvu yachipulumutso ya Yesu Khristu.

**MADZI AIMIRA MWAZI NDI MAZUNZO A KHRISTU**

Chipatso cha vinyo chimene Yesu adagwiritsa ntchito adali wochokera ku zipatso za mphesa. Chipatso chimaimira mwazi umene Khristu adakhetsa pamtanda (Mateyu 26:28). Poyamba mphesa ziyenera kufinyidwa kuti zitulutse madzi opangira vinyo. Khristu adakwapulidwa, kumenyedwa ndi kupachikidwa kuti kudzera mu mwazi wake tikhale ndi chikhululukiro cha uchimo. Mwana aliyense wa Mulungu ali ndi chiyanjano kudzera mu mwazi wa Khristu (1 Akorinto 10:16).

**MMENE MUNGACHITIRE MWAMBO WA MGONERO**

Pali njira zambiri zimene mipingo imatsata pochita mgonero. Nkofunika kuti cholinga chenicheni cha chizindikiro cha mgonero chisatayike pamene tikuchita mgonero. Yesu

*(Yapitirira pa tsamba 6)*

*(Kuchokera pa tsamba 5)*

poyamba adatenga mkate wopanda chotupitsa. Anawudalitsa, naunyema kenaka anagawira akuphunzira (Marko 14:22). Iyi ndiyo ndondomeko ya m'baibulo ya mmene tingachitire mgonero. Matchalitchi ambiri amagwiritsa ntchito mabisiketi a phwanthiphwanthi ndipo izi zimapangitsa kuti chizindikiro chakunyema mkate chitaike. Kenaka, Yesu "anatenga chikho, ndipo pamene adayamika, anapereka kwa iwo; ndipo iwo onse anamweramo" (Marko 14:23). Padali chikho chimodzi chimene onse adamwera. Izi sizitanthauza kuti tonse timwere chikho chimodzi koma ndi chizindikiro chabe chimene chili ndi tanthauzo lalikulu ku uzimu. Anthu a Mulungu adamwera chikho chimodzi cha mazunzo a Ambuye wathu. Ichi chitanthauza mchitidwe wakugawana. Pomaliza pa mgonero woyamba, akuphunzira adayimba nyimbo nachoka (Marko 14:26). Pali mdalitso wapadera mwambowu ukatsatidwa ndipo anthu a Mulungu achoka pa mgonero wa Ambuye monga momwe adachitira akuphunzira akale. Sikoyenera kuleka kapena kusintha ndondomeko ya m'Baibuloyi.

#### KUCHITA MWAMBO WA MGONERO KOSAYENERA

Mpingo wa Akorinto sudachite mwambo wa mgonero wa Ambuye moyenera. Paulo akuwadzudzula ndikuwapatsa malangizo a mmene ayenera kuchitira (1 Akorinto 11:20-22, 34). Mpingo umatenga nthawiyi ngati yochitira madyerero ndi chisangalalo. Iwo sadazindikire za tanthauzo la mgonero. Paulo adawalangiza kuti azikadya kunyumba ndipo kuti mgonero wa Ambuye sunali wothetsera njala ya munthu. Mgonero udali nthawi yakukumbukira Khristu pakuchita mwambo.

#### MGONERO NDIWO WA ANTHU OKHULUPIRIRA

Mgonero wa Ambuye ndiwo mwambo wa anthu owomboledwa (1 Akorinto 11:27-32). Paulo adanena kuti aliyense akadya mkate ndi kumwera chikho mosayenera achimwira thupi ndi mwazi wa Ambuye. Aliyense ayenera kudzifufuza asanadye nawo mgonero; ndipo iyi si ntchito ya utumiki. Mgonero ndiyo nthawi yakuti aliyense adzifufuze yekha osawerengera za chipulumutso chake. Mgonero ndiyo nthawi yakulingalira mwapadera za moyo wanu, khalidwe lanu, machitidwe anu ndi kapenyedwe kanu ka zinthu. Ambiri mu mpingo adaali odwala, ofoka, komanso kumwalira kumene chifukwa samaikapo mtima pakudya mgonero wa Ambuye. Kusalabadiraku sikuti kumapangitsa kuti iwo atayike kwamuyaya koma kuti zimautsa chiweruzo cha Mulungu. Mulungu amawalanga kuti asaweruzidwe kwamuyaya monga mmene linachitira dziko lapansi (1 Akorinto 11:29, 32). Mgonero wa Ambuye ndi simwambo wachibwana ndipo pafunika kuuchita mosamala kwambiri komanso kuupatsa ulemu waukulu.



> "Mpingo wa Mulungu ukhulupirike pokumbukira…Mgonero womaliza wa Ambuye mpaka Iye adzabweranso."

#### ANTHU A MIBADWO AKULAMULIDWA KUTI AUSUNGE MWAMBOWU

Kudya mgonero wa Ambuye ndiwo mwambo umene atumwi amachita koma umene mibadwo yonse imayenera kutsata. Yesu adaphunzitsa mpingo wake kuti "asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu" (Mateyu 28:20). Langizo la Paulo linali lakuti "kusunga miyambo monga momwe ndinapereka kwa inu" (1 Akorinto 11:2). Yesu adati "chitani ichi" (1 Akorinto 11:25). Mpingo wa Mulungu ukhale wokhulupirika pokumbukira mazunzo a Khristu pochita mwambo wa mgonero wa Ambuye mpaka Iye adzabweranso.

-mws

# Funso ndi Yankho

## Kodi lamulo la mgonero wa Ambuye tilikumbukire kangati?

MPINGO ADAULAMULA KUTI UTSATE LAMULOLI. ANTHU AMENE SADYA NAWO MGONERO ALI NDI ZOSOWA ZAWO ZA UZIMU ZIMENE AYENERA KUPEMPHA AMBUYE. Yesu sadauze mpingo kuti mwambo wa mgonero azichita kangati. Iye adati, "Pakuti nthawi zonse mukadya mkate uwu ndi kumwera chikho…" (1 Akorinto 11:26). Zili kwa munthu yekha kusankha kuti ayenera kudya mgonero kangati. Chofunika kudziwa ndicho chakuti Yesu adanena lamuloli potsatira mwambo wa Paska umene umachitika kamodzi pachaka.

Anthu ena amadya mgonero kamodzi kapena kangapo pa mulungu. Ngakhale uku sikulakwa, vuto nlakuti ichi chingakhazikike ngati mwambo chabe. Vuto lina nlakuti anthu ena amakhala ngati akutetezeka akamadya mgonero kawirikawiri. Munthu sadzapulumuka chifukwa chakudya mgonero. Munthu amapeza chipulumutso mwachisomo chifukwa cha chikhulupiriro chimene chimapangitsa kuti munthu akhale ndi moyo wachiyero.

## Kodi ana adye mgonero?

MAWU A MULUNGU SANENA ZA MSINKHU WOYENERA KUTI MUNTHU ADYE NAWE MGONERO KOMA AMANENA ZOYENERA KUTI TIZITSATIRE. Mawu akunena momveka kuti "munthu adziyese yekha" (1 Akorinto 11:28). Anthu oyenera kudya mgonero ndiwo okhawo amene adapulumutsidwa. Mwana wachaka chimodzi kapena zaka ziwiri alibe maganizo okhwima otha kudziyesa yekha. Monga ubatizo wa ana umatsutsana ndi chiphunzitso cha Baibulo chimodzimodzinso mgonero wa ana umatsutsana ndi chiphunzitso cha Baibulo. Ndi udindo wa makolo kumudziwa mwana wawo ndiponso nthawi yomwe mwana ayenera kudya nawo mgonero. Ngakhale kuti makolo ayenera kulera ana awo m'makhalidwe a Mulungu, mgonero ndi chikumbutso chapadera cha anthu okhawo amene adabadwa kwatsopano. Ana ayenera kuzindikira kuti kudya mgonero sichinthu chamasewera ndipo alemekeze mwambowu. Mwana adye mgonero pokhapokha atapulumutsidwa.

## Kodi chiphunzitso cha Chiroma chimati chiyani?

CHIPHUNZITSO CHA CHIROMA CHABODZA CHOKHUDZA MKATE NDI VINYO. Chiphunzitso ichi chimene amachilalikira a Mpingo wa Chiroma chimanena kuti panthawi ya mwambo wa misa, "mkate ndi vinyo" zimasintha kukhala thupi ndi mwazi wa Khristu weniweni ngakhale kuti sizioneka choncho. Chiphunzitso ichi amachitenga pa mawu a Yesu amene adanena kuti "ili ndi thupi langa" ndiponso "uwu ndi mwazi wanga" (Mateyu 26:26, 28).

Yesu samanena za thupi lenileni kapena mwazi weniweni. Iye amayankhula chining'a. Yesu amayerekeza thupi ndi mkate ndiponso mwazi ndi vinyo. Mu buku la Akorinto 11:26, iye adanena kuti "nthawi zonse mukadya mkate uwu…." Adauza akuphunzira ake kuti adye mgonero wa Ambuye "chitani ichi chikumbukiro changa" (Luka 22:19). Izi zitanthauza kuti thupi lake silinali mu mkate wa mgonero. Mkate ndi chipatso cha vinyo ndizo zizindikiro chabe za thupi ndi mwazi wa Khristu.

-mws



**KODI MUKUDZIWA?**

*Ndipo atayimba nyimbo, anaturuka, namuka ku phiri la Azitona.*
—Marko 14:26

Ayuda adachita Pasaka pakuyimba nyimbo ya Aleluya. Nyimboyi ichokera pa Masalimo 113-118 ndipo amayigwiritsa ntchito pa kutamanda ndi kuthokoza. Masalimo 113-114 amayimbidwa kawirikawiri asanadye chakudya ndipo Masalimo 115-118 atatha kudya chakudya.

Palibe chikayiko kuti Yesu ndi akuphunzira amayimba nyimboyi asanapite ku phiri la Azitona.

Mau a pa Nyengo Yake

# Chiyanjano cha zowawa za Yesu

*Ndiyesa zonse zikhale chitaiko ....kuti ndikamzindikire Iye, ndi mphamvu ya kuuka kwake, ndi chiyanjano cha zowawa zake, pofanizidwa ndi imfa yake.*
—Afilipi 3:8-10



Mtumwi Paulo adayesa zonse za moyo uno ngati zopanda ntchito kuti apeze kotheratu moyo ndi mphamvu ya Khristu. Paulo adamudula khosi chifukwa cha chikhulupiriro chake. Malinga ndi zomwe iye adalemba, ndikukhulupirira kuti Paulo adachilandira ichi monga mowe adalandilira mavuto ena onse mmoyo mwake.

Ambuye Yesu adasiya ulemerero wake Kumwamba, nabwera kudziko lino lochimwa kuti aone umoyo wa dziko lapansi, ndi kudzipereka nsembe ya tchimo lathu. Tili naye ngongole imene sitingathe kubweza chifukwa cha mphatso ya chipulumutso ndi moyo wosatha. Ndi chinthu cha ulemu komanso mdalitso kumwera chikho cha mazunzo a Khristu.

Origen, mmodzi mwa akhristu otchuka a mu mpingo woyamba ananena kuti Mtumwi Petro adadziona wosayenera kuphedwa ngati Mbuye wake, kotero kuti anapempha kuti amupachike chozolika.

Mazunzo athu sangafanane ndimazunzo a Khristu. Adakanidwa, adaperekedwa, adakanidwa, adamunamizira, adamunenera bodza, adamulavulira malovu, adamukwapula ndi kumupachika. Ha! mwana wa Mulungu, usakhumudwe kapena kugwa mphwayi pa nthawi ya mazunzo ndi mayesero. "Koma kondwerani ngakhale muzunzika naye Khristu kuti pa vumbulutso la ulemerero wake, mukakondwere kwakukulukulu" (1 Petro 4:13).

-mws

**KUTI MUTIPEZE**

The Gospel Truth
605 Bishops Ct.
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org